# Global Storybooks

globalstorybooks.net

## Nthochi za Agogo

Ursula Nafula
Catherine Groenewald
David Sani Mwanza

This work is licensed under a Creative Commons Attribution 3.0 International License.
https://creativecommons.org/licenses/by/3.0

# Nthochi za Agogo

Ursula Nafula
Catherine Groenewald
David Sani Mwanza

4

Chichewa ny

Dimba ya agogo inali yabwino, ili ndi mapila ndi manyuchi ndi tute. Koma zabwino kuposa zonse zinali nthochi. Angakhale kuti agogo anali ndi ana azukulu ambiri, ndinaziwa kuti ndinali wapa mtima wao. Anali kundiitana kawiri kawiri kunyumba yao. Anandiuza zachisinsi. Koma kunali chisinsi chimozi chomwe sanandiuze: kwamene anasungila nthochi kuti zipsye.



M’madzulo tsiku lija, amai ndi atate ndi agogo anandiitana. Ndinadziwa chomwe anali kundiitanira. Utsiku uja pamene ndinagona pansi, ndinadziwa kuti sinzakabwelezapo kubela agogo, makolo anga kapena munthu wina ali yense.

Tsiku lotsatirapo inali tsiku lopita ku msika. Agogo anauka msanga. Anali kutenga nthochi zakupsya ndi tute kukagulisa pa mtsika. Sindinafulumire kuwatsatira tsika lija. Koma sindinakwanise kukhala kopanda iwo.



Tsiku lina, ndinaona nswanda ili pa dzuwa panja pa nyumba ya agogo. Pamene ndinafunsa nchito yake ya nswanda, yankho inali yakuti, “Ndi nswanda yanga yamasenga.” Pafupi ndi nswanda, panali mayani a nthochi yomwe agogo anayikamo nthawi ndi nthawi. Ndinali ndi mafunso ambiri. “Kodi mayani ndi achani? ndinafunsa. Yankho yomwe anandipasa ndiyakuti, “ndi mayani anga a masenga.”

Chinali chosangalasa kuona agogo anga, nthochi, mayani a nthochi ndi nswanda yaikulu. Koma agogo ananditumа kutipita kwa amai anga. “Agogo, chonde, lekani ndikhale nainu pamene mukonzeka…” “Osachita nthota, mwana, chita zomwe ndakuuza,” anakakamiza. Ndinanyamuka ndi liwiri.



Tsiku lotsatirapo, pamane agogo anali mu dimba kutenga ndiwo zamasamba, ndinalowa munyumba mwakabisila ndikuona nthochi. Pafupi fupi zonse zinali zakupsya. Ndinatengapo zinai. Pamene ndinali kupita ku chotseko mwakachetechete, ndinamva agogo akhosomola panja. Ndinabisa nthochi mu delesi langa ndipo ndinawapitilira.

Tsika losatirapo pamene agogo anabwela kutandalira amai, ndinathamgira ku nyumba yao kukaonanso nthochi. Panali zina zomwe zinapsya kwambiri. Ndinatengapo imozi ndi kuibisa mu delesi yanga. Pambuyo pakutseka nswanda, ndinapita kuseli kwa nyumba ndipo ndinadya nthochi mofulumira. Inali nthochi yonzuna kuposa nthochi zonse zomwe ndinalawapo.



Pamene ndinabwelera, agogo anali khale panja koma analibe nthochi . “Agogo, kodi nswanda ili kuti, nthozhi zonse zili kuti, ndipo ali kuti…“Koma yankho yomwe anandipatsa ndi yakuti, “zonse zili mu malo anga amasenga.” Zinali zokhumudwitsa.

Patapita masiku awiri, agogo ananditima kukatenga ndodo yao kuchoka ku chipindi chao chogonamo. Pamene ndinasegula chiitseko, ndinamva nthochi kununkhira. Mukati mwa chipinda munali nswanda ya masenga ya agogo. Inali yobisika ndi gombeza wakale. Ndinasegula ndipo ndinamva kunkhira kokoma.



Mau a agogo anandiopsya pamene anati, “Uchita chani? Fulumira bweletsa ndodo.” Ndinapita panja mofulumira kupeleka ndodo. “Umwetulira chani?” Agogo anafunsa. Funsa yao inandididzwisa kuti ndinali kumwetulira nthochi zomwe ndinaona mumalo a masenga.